



Mbali ina ya nkhalango ya Matandwe

# Ateteza nkhalango ya Matandwe

WOLEMBA:  
MARTIN GELA JNR

**T**/A Malemia m'boma la Nsanje yayamikira akuluakulu a bungwe la Shire Valley Transformation Project (SVTP) pantchito yomwe akugwira yosamalira malo wotetezedwa a nkhalango ya Matandwe m'bomalo.

Mfumuyo yapempha mafumu ndi anthu womwe azungulira nkhalangoyi kuti agwirane manja pofuna kuteteza nkhalangoyi yomwe yati ndi yofunika kwambiri.

Mfumu Malemia idati: "Kale ife timaona nyama za m'nkhalango moga mbira, anyani, agwape, akambuku ndi zina koma lero lino ndi mbiri yakale chifukwa anthu anayamba kulowa m'nkhalangoyi ndi kuyamba kumalimamo zomwe sizoyenera."

Iwo adati kupatula kuona nyama, nkhalango ya Matandwe inkapereka zipatso zambiri za mtchire moga mpinjipinji, matowo, magwafa, mulusi, bwemba komanso mankhwala wothandiza kwambiri omwe amatchedwa kuti thabalaba womwe azungu ku Germany komanso anzathu ku India amakonda kugwiritsa ntchito komatu amakatenga kunoku.

T/A Malemia adati



ZITHUNZI: HOLYCE KHOLWA

**A Malemia: Idali yovalira bwino**

pomwe nkhalangoyi inali yovalira bwino ku Nsanje kumagwa mvula yabwino komanso ngozi zogwa mwadzidzi kunali ndiye iwo ayamikira a SVTP polingalira kuti aike ndalama zotetezera nkhalangoyo koma adachenjeza kuti athana ndi wina aliyense yemwe angapezeke akulima kapena kuotcha makala m'nkhalango yomwe ndi mbali imodzi ya Kirk Range yomwe idakathera ku Dzalanyama m'boma la Lilongwe.

Agulupu a Mchacha omwe amakhala ku Chididi yomwe ndi gawo

lina la nkhalangoyi ati aza anthu awo kuti kusapezeke wolima m'nkhalangoyi kapena kuotcha makala ndipo anati akugwira ntchito limodzi ndi akuluakulu woona za nkhalango m'bomalo.

Mmodzi wa akuluakulu woona za nkhalango kumeneko a John Banda adati akuyesetsa kugwira onse omwe akupezeka atapalamula milandu m'nkhalangoyo pansu pa ndondomeko ya ntchito ya SVTP.

A Banda adati: "Takwanitsa kutengera kubwalo la milandu

nkhani zoposa 20 ndipo anthu akhala akulandira zilango moyenera ndi momwe anapalamula. Kulima, kukhala komanso kuononga zachilengedwe moga kudula mitengo ndi kuotcha makala ndi milandu yomwe ikuchulukira koma ndi mgwirizano wa mafumu tikuona kuti zikutheka kuti anthuwa azimangidwa ndi kulandira zilango."

Mmodzi mwa akuluakulu a SVTP, a Stanley Khaila adati pofuna kuteteza nkhalango zomwe zili mmalo momwe akugwira ntchito akhala akugawa mbuzi zomwe anthu amagawana ndipo panopa anakwanitsa kufikira anthu 220 ozungulira nkhalango ya Lengwe ku Chikwawa ndi mbuzi 1 100 komanso Mwabvi ku Nsanje komwe adapereka mbuzi 605 kwa anthu 121.

SVTP ikugwira ntchitoyi ndi thandizo la ndalama kuchokera ku Global Environment Facility (GEF) ndi ndalama zokwanira \$5.6 miliyoni (K5.6 triliyoni) ndipo akuteteza nkhalango za Matandwe, Mwabvi, Lengwe, Majete, Elephant Marsh, Thambani komanso Thyolo Escarpment komwe mitsinje yambiri yothira mu Shire ili ndi magwero ake. ■

**BWALO LA  
ULIMI**



WOLEMBA: ANDREW SAUKANI

## Nsanamira m'chaka cha usodzi, alimi a nsomba

2022 ndi chaka choganizira asodzi ndi alimi a nsomba ang'onoang'ono, International Year of Artisanal Fisheries and Aquaculture (lyafa: 2022). Bungwe la Food and Agriculture Organisation (FAO) ndi limene likutsogolera zochitika zonse zokumbukira izi mothandizana ndi nthambi ya usodzi ndi mabungwe ena.

Izi zikuchitika m'maiko onse pamutu oti Small in Scale, Big in Value kutanthauza kuti zochitika mwapang'ono koma zopindulira ambiri.

Pokondwerera chakachi pakhala pakuchitika zosiyanasiana zozindikiritsa adindo ndi anthu onse kufunika kwa ulimi wa nsomba komanso usodzi makamaka wa an'gonoan'gono.

Izi zikumbukiridwa potsata nsanamira zisanu ndi ziwiri zimene zitambasulidwe motere. Nsanamira yoyamba ndi kusamalira zachilengedwe (biodiversity conservation) kuti chikagwiritsidwe mosamala. Kusamalira zachilengedwe kudzatanthauza kupitilira kupindulira chifukwa pamene nsomba zimakhala m'madzi, madzi tsopano ali pachiopezo pomatayilamo zinyalala, mafuta komanso dothi lochuluka likukwirira nyanja ndi mitsinje. Nsanamira yachiwiri ndi kuonetsetsa kuti anthu akupindula pachuma kudzera mu nsomba (economic sustainability).

Nsomba tisamangoziona kumbali ya asodzi ndi alimi okha komanso tizindikire kuti palinso anthu ambiri amene amaigwira nsombayi isanafike poti yadyedwa.

Pali okonza ndi kugulitsa nsomba, onyamula nsomba komanso okonza zida zophera nsomba moga mabwato. Anthu onsewa amadalira nsomba pamoyo wawo. Nsanamira yachitatu yatsindika kusamalira miyoyo ya anthu ogwira ntchito zokhudza nsomba (social sustainability) kuti nawonso akathe kumalandira chisamaliro moga wina aliyense pa zamaphunziro, umoyo wabwino, kutetezedwa ndi malamulo mofanana ndi nzika ina iliyonse.

Nsanamira yachinayi ikulimbikitsa ulumuliro wabwino (good governance) poonetsetsa kuti zofuna za asodzi ndi alimi a nsomba ang'onoang'onowa zikukwaniritsidwa ndipo eni ake akutengapo gawo pomanga mfundo ndi ndondomeko mmene akufunira ntchito zawo ziyendera. Apa mpamene alimi a nsomba ndi asodzi akulimbikitsidwa kumakhala m'magulu.

Gawo lachisanu ndi kulimbikitsa amai kutengapo mbali pa usodzi (gender equity and equality) kuti azitha kugwira mbali ina iliyonse ya usodzi mosasalidwa komanso mosiyantsidwa ndi abambo. Usodzi opha nsomba panyanja ukuchitika kwambiri ndi abambo pamene amayi ambiri ndi amene akusamalira nsomba ku madamu ndi mabizinesi ena a nsomba motere amayiwa asatchingidwe, kapena kuwaphera mafulu awo kuti apezze nsomba.

Pali chikhulupiliro kuti pamene mayi mmodzi akupindula ndi bizinesi ya nsomba, anthu ena oposera asanu amathandizika nawo. Nsanamira yachisanu n'chimodzi ndi (food and nutrition sustainability) poonetsetsa kuti nsomba zikuthandiza pakapezedwe kachakudya komanso kulimbikitsa thanzi pakati pa anthu.

Nsanamira yomaliza ndi kulimbikitsa kupirira (resilience) pamene nyengo ikusintha, chilengedwe chikusakazika koteru ulimi wa nsomba ndi usodzi zichilimike ndi kusinthaku koteru zikapitilire. ■

Mafunso: saukaniandrew@gmail.com